

LAUDATO SI`



Chipangano cha Mpingo wa Katolika
ndi Nyengo: *Kusamalira chilengedwe,
kusamalira anthu osauka.*



Laudato Si` mwachidule mokhudzana
ndi kusamalira chilengedwe ndi dziko
lathu.

Mawu Othokoza

Bungwe la ma Episikopi muno M'malawi likuthokoza ma bungwe ali mmusiwa kamba kostogolera ntchito yomasulira Kalata yokhudzana ndi zachilengedwe "Laudato Si" kuchokera ku chingelezi kupita mu Chichewa. Kalatayi idalembedwa ndi A Papa a Francis mu chaka cha 2015.

- Jesuit Centre for Ecology and Development (JCED)
- Trocaire
- Catholic Development Commission of Malawi (CADECOM)



Zam'katimu

MUTU 1: Chikuchitika nchiyani m'dziko lathu?

Tsamba 3)

MUTU 2: Mthenga Wabwino wokhudza

Chilengedwe (Tsamba 7)

MUTU 3: Munthu ndiye gwero lakuwonongeka kwa chilengedwe (Tsamba 9)

MUTU 4: Ubale wa zachilengedwe (Tsamba 11)

MUTU 5: Njira zothanirana ndi vuto la

kuwonongeka kwa chilengedwe(Tsamba 13)

MUTU 6: Maphunziro okhudza chilengedwe potengera chiphunzitso cha Mulungu (Tsamba 15)

MAU OYAMBIKIRA

M'kalata yake yotchedwa *Laudato Si'*, Papa Francis akupereka uthenga wake wokhudza chilengedwe kwa “munthu wina aliyense wokhala m'dziko lapansi” (3-4). M'kalatayi, iye akutsindika mfundo zotsatirazi:

- Masompheya ogwirizana ndi amene iye adalowa m'malo mwao (§§ 3-6) ndiponso mogwirizana ndi amene sali Akatolika ndi magulu a anthu ena pa dziko lapansi (7-9).
- Iye akuwonetsa kuti buku la *Laudato Si'* lidalembedwa potengera moyo wa Francis Woyera wa ku Assisi, amene anakonda zachilengedwe ndipo adasanduka nkhoswe yolimbikitsa chisamaliro cha chilengedwe. Iye akutsindika za kufunikira kwa chiphunzitso cha Mpingo ngati maziko abwino osamalira chilengedwe. M'mau ake, iye akuti: “Ngati tiwona chilengedwe ndi nyengo koma mosazindikira ulemelero wake ndiponso mosadabwa kanthu, komanso ngati sitilankhula za ubale wathu umene ulipo pakati pa ife ndi chilengedwe, ndiye kuti tidzasanduka anthu ogwiritsa ntchito chilengedwecho moipa. Tidzasandukanso anthu osakaza ndi owononga chilengedwe mosaganizira zakutsogolo. Ku mbali inayi 'ngati tikonda ndi kusamalira zolengedwa zonse ngati adindo, ndiye kuti chilengedwe chidzatisamaliranso ife ndipo moyo wathu udzayenda bwino' (§II)

Papa Francis akupempha anthu onse kuti pakhale kukambirana za momwe tingakonzere ndi kusamalira chilengedwe chimene ndi tsogolo la dziko lapansi (14)

MUKAFUNA KUDZIWA ZAMBIRI:

Werengani kalata yonse yotchedwa *Laudato Si`* imene imafotokoza za chisamaliro cha chilengedwe ndi dziko lathu v2.

Vatican.va/content/Francesco/en/encyclicals/documents/papa-francesco_20150524_enciclica-laudato-si.html

Kapena *Laudato Si`*

www.catholicclimatecovenant.org/resources/laudato-si.



MUTU 1: CHIKUCHITIKA NCHIYANI M'DZIKO LATHU? —————

Papa Francis akuwona kuti, masiku ano kuli mavuto aakulu m'dziko lathu okhudza chilengedwe. Ena mwa mavutowo ndi monga: Kuwonongeka kwa mpweya ndi kusintha kwa Nyengo (20-26) kusowa kwa madzi abwino akumwa (27-31). kuwonongeka kwa chilengedwe mwanjira zosiyanasiyana (32-42): kutsika ndi kulowa pansu kwa moyo wamunthu ndiponso kuwonongeka kwa moyo ndi chikhalidwe pakati pa anthu (43-47); komanso kusiyana kwakukulu pakati pa anthu olemera ndi osauka.

Pa nkhani ya kusintha kwa nyengoyi, Papa Francis:

- Akutsindika kuti nyengo ndi chinthu chabwino, ndiponso chokomera munthu aliyense. Iye amazindikira kuti, zomwe akatswiri asayansi ambiri akunena kuti, kutentha kwa dziko lapansi komwe kwakhala kukuchitika m'zaka zapitazi, ndi chifukwa cha kuchuluka kwa mpweya woipa mumlengalenga wotchedwa (carbon dioxide, methane, nitrogen oxide ndi wina wotero). Mpweya woipawu umabwera chifukwa cha machitidwe oipa a munthu. (23).
- Papa Francis akunenetsa kuti, kusintha kwa nyengo kukukhudza dziko lonse lapansi ndipo zotsatira zake ndi zoipa kwambiri mokhudzana ndi nyengo, moyo ndi chikhalidwe cha anthu, chuma, ndale ndiponso kapezedwe ka zinthu zomuyenerera munthu aliyense. Kuwonjezera apa, iye akudandaula kuti anthu osauka, amene satenga nawo mbali yaikulu pakusakaza chilengedwe ndi kusintha kwa nyengo, ndi amene akupezeka pachiwopsezo chachikulu m'moyo wao (25).
- Papayo akuzindikira kuti nkofunika kuti m'zaka zocheza zikudzazi payenera kukonzedwa mfundo zothandiza kuchepetsa kufala kwa mpweya woipa wa *carbon dioxide* ndi mipweya ina yoipa. Mipweya yoipayi itha kuchepetsedwa kwambiri; mwachitsanzo, pochepetsa kugwiritsa ntchito mafuta ndi kuyesa kupeza njira zina zatsopano zopangira mphamvu za magesti kaya kuphikira monga mphamvu ya dzuwa (26).
- Iye akudzudzula anthu amene amati,



akummwera. Kusiyanaku kumachititsa kuti maiko osauka azilephera kusamalira ndi kugwiritsa ntchito bwino zachilengedwe chifukwa alibe kuthekera kopezera mwapafupi njira zina zopezera mphamvu monga magetsi (51),

- Papayu akudzudzula maiko kaamba kosachitapo zakupsa mofulumira pofuna kuti chilengedwe chisapitirire kuwonongedwa. Iye akuti maiko ena amakhala ngati sakuwona vutoli kaamba kot chiidwi chao chili pa kupeza chuma chambiri kudzera mkuwononga zachilengedwe mwachisawawa (54)






MUTU 2: MTHENGA WABWINO WOKHUDZA CHILENGEDWE

Papa Francis watchulapo zinthu zingapo zimene Chikristu chimaphunzitsa. Zina mwa zimenezi ndi zotsatirazi:

- Mulungu adalenga zinthu zonse ndipo adazilenga zonse zabwino (65-69).
- Anthu adalengedwa mwapadera napatsidwa udindo wa kukhala akapitawo oyang'anira chilengedwe chonse m'malo mwa Mlengi wachikondi (67-68).
- Zolengedwa zonse ndi zodabwitsa (misteri) chifukwa mwa izo, ngakhale zili zosiyanasiyana, koma umodzi wao umasonyeza poyera ulemelero wa Mulungu Mlengi (76-92).
- Iye akutsindika kuti, maphunzitso a Mpingo wa Katolika, amati, ufulu pa nkhani yokhala ndi chuma ndi pamalonda, si chinthu choti munthu nkuchigwiritsitsa ngati chakechake, ai, koma kuti zonse zidalengedwa kuti zitetzedwe ndi kupititsa patsogolo moyo wa anthu onse pa dziko lapansi (93).
- Tsogolo la zolengedwa zonse liyenera kukwaniritsidwa m'misteri ya Khristu (99)

Mwachidule, Papa Francis akufuna kutsindikira kuti, kuwonongeka kwa chilengedwe kukuchitika chifukwa cha tchimo lomwe lidasokoneza ubale wa zolengedwa ndi Mulungu. Ubalewu udasokonezekanso pakati pa anthu ndiponso pa dziko lonse lapansi (66). Ubale wosokonezekawu ndi umene ukuchititsa kuti pakhale vuto la kusintha kwa nyengo kaamba koti munthu ndi wodzikonda chifukwa amadzipatsa mphamvu ndi kukhala ngati Mulungu amene nakana kuvomereza umunthu ndi kufooka kwake. Ndi kaganizidwe kotereka kamene kamachititsa munthu kuti azitenga lamulo la Mulungu kukhala ngati lake ndi kudziyesa ngati wolamulira chilengedwe mwachisawawa (Gen 1:28). Munthu amaganiza kuti pamene Mulungu adamulenga kuti asamalire zolengedwa zonse, adampatsa mphamvu zowononga chilengedwe m'malo mochisamalira ngati mphatso yaikulu yochokera kwa Mulunguyo (Gen.2:15)





MUTU 3: MUNTHU NDIYE GWERO LA KUWONONGEKA KWA CHILENGEDWE

**Mowunikiridwa ndi chikhulupiriro
Chachikhristu, Papa Francis akufotokoza kuti
munthu ndiye gwero la kuwonongeka kwa
chilngedwe, Iye:**

- Akudzudzula chiphunzitso chimene chimaika munthu pamwamba pa zolengedwa zina zonse molakwika (115 -118).
- Iye akutsindikanso mwachimvekere kuti anthu oganiza motere amatenga chilengedwe ngati chopanda pake ndi chosafunikira pokhapokhapo ngati chikuwapindulira (118, 122).
- Komanso Papa Francis akudzudzula anthu amene amaona chitukuko cha zipangizo zamakono ngati chowathandiza kupeza phindu mosalabadira zotsatira zake zoipa pa moyo wamunthu. Amatinso, chuma chimaposa chitukuko cha moyo wa munthu ndipo pa chifukwa ichi, atha kugwiritsa ntchito chilengedwe mosalabadira (109).

- Iye akubwereza kutsindika za kufunika kwa chiphunzitso cha Mpingo Wakatolika chimene chimati, msika wa zinthu zolengedwa sichitsimikizo chakuti munthu atha kutukuka m'moyo wake wonse mosapatula wina aliyense pa dziko lapansi, ai.
- Koma chitukuko chenicheni chiyenera kuwongoleredwa ngati moyo wa munthu sukutetezedwa ndi kupita patsogolo (Ibid)
- Iye akubwerezanso kunena kuti, mgwirizano ngofunika pakati pa zolengedwa zonse ndipo potero, mgwirizanowu umalimbikitsa chisamaliro cha chilengedwe ndi chitetezo cha munthu kuphatikizapo chitetezo cha ana osabadwa, ulemerero wa munthu makamaka osauka, aulumali ndi ena osalabadiridwa (117, 120, 137).



MUTU 4: UBALE WA ZACHILENGEDWE

Papa Francis akufotokoza za ubale ndi mgwirizano wa zachilengedwe ndipo akunena kuti:

- Ndi chinthu chosakayikitsa konse kuti zachilengedwe zimadalirana ndipo izi, Papa Francis akuzinena mobwerezabwereza (138). Iye akuti, izi ndi zoonza mokhudzana ndi zolengedwa zonse kuphatikizapo munthu ndi zonse zokhudza moyo wake monga maphunziro, chuma, moyo wathanzi, ulamuliro ndi kayendetsedwe ka dziko ndi zinthu, chikhalidwe ndi zina zonse zochitika tsiku ndi tsiku pa moyo wamunthu (139-155).
- Iye akubwereza kuti kusamalira chilengedwe kumayenderana ndi kupititsa patsogolo ndi kutukula moyo wa anthu osauka omwe kawirikawiri amakhudzidwa ndi kuwonongeka kwa chilengedwe (158).

- Iye akupitiriza kutsindika kuti, chifukwa cha kuwonongeka kwa chilengedwe ndi nyengo, pakuyenera kukhala chilungamo ndi umodzi, kuti pakhale kudzipereka kwathunthu pofuna kukwaniritsa ubwino wokhalira anthu onse kuphatikizapo ubwino wa ‘mibadwo yam’tsogolo ” (159).




MUTU 5: NJIRA ZOTHANIRANA NDI VUTO LA KUWONONGEKA KWA CHILENGEDWE

Mfundo yothandiza kuwongolera zinthu yomwe Papa Francis akufotokoza pa mutu 5, ndi yokhudza Maphunzitso a Mpingo wa Katolika amene amati, mavuto akuyenera kuthetsedwa kuyambira ndi munthu wammunsi ku dera lake. Adindo akuluakulu atengepo mbali pokhapokhapo atapereka mpata kwa anthu kuti adzithandize okha pofuna kuteteza ndi kutukula ubwino wa munthu aliyense.

Ndipo Papayo akutsindika kuti:

- “Zipangizo zamakono zomwe zimagwiritsa ntchito mafuta kapena malasha komanso gasi zimabweretsa mpweya woipa, ndipo anthu ayenera kusiya kugwiritsa ntchito zinthu zimenezi mwamsanga” (165).
- Kufikirira pa nthawi imene anthu adzakwaniritse kugwiritsa ntchito njira zosawononga chilengedwe (renewable energy), ndibwino kusankha ndi kumagwiritsa ntchito zipangizo zosadzetsa mavuto aakulu owononga chilengedwe (Ibid).
- Ntchito yopeza zipangizo zamakono zosagwiritsa ntchito mafuta kapena malasha (renewable energy), ikuyenera kuyambika mwamsanga. Kuti izi zitheke, pafunika kuti maiko olemera athandize maiko osauka ndi chuma chokwanira komanso upangiri wabwino kuti nawonso apeze njira zothandiza kugwiritsa ntchito zinthu zosawononga chilengedwe. Papa Francis akuti, mtengo wa zipangizo zofunikira pa ntchitoyi ukuyenera kukhala wotsika kuti maiko osauka athe kugula makamaka poganizira zotsatira zoipa za kusintha kwa nyengo” (171).
- Ngakhale patakhalana njira zokhwima zothanirana ndi mavuto a kusintha kwa nyengo tsopano, maiko ena osauka adzasowabe thandizo lowathandiza kuti nawonso apeze mwai wothana ndi mavuto amene awakhudza kale (170).
- Papa Francis akutsindika za kufunikira kotali aliynse atengepo mbali m’maiko osiyanasiyana pa nkhani yosamalira chilengedwe. Pobwereza mau a Aepiskopi a ku Bolivia amene adati: “maiko amene adapindula ndi ntchito zamafakitare ndipo ndi amenenso amatulutsa mpweya woipa kwambiri, ali ndi udindo waukulu woipeza mayankho ku mavuto amene adadza chifukwa cha m’chitidwe wao” (170).
- Papa Francis akuti pakhale kukambirana moona ndipo maiko osauka akuyenera kutengapo mbali pa zokambiranazi (183). Iye akutsindikanso mfundo yothandiza kupewa vuto lakuwonongeka kwa chilengedwe, mwakuti ngati pali projekiti imene zotsatira zake zitha kuwonga chilengedwe kapena kudzetsa mavuto osaneneka mtsogolo, ntchitoyo iimitsidwe kapena isinthidwe kachitidwe kake (186).



MUTU 6: MAPHUNZIRO OKHUDZA CHILENGEDWE POTENGERA CHIPHUNZITSO CHA MULUNGU

A Papa a Francis:

- Akupempha kuti munthu aliyense atembenuke mtima payekhapayekha komanso ngati gulu lonse la mtundu wa anthu ndi kusiya mtima wodzikonda. Akupemphanso anthu onse kuti akhale ndi makhalidwe oganizira chilengedwe ndi ubwino wa anthu onse. Izi ziyenera kukhudza anthu okhulupirira Mulungu ndi ena onse pa dziko lapansi (202-215).
- Iye akutchulaponso magulu ena a anthu amene ali ndi mtima wongofuna kudziwunjikira zinthu zambiri ndipo amafuna kuwongolera kachitidwe ka malonda osiyanasiyana pofuna kupeza phindu lalikulu ndi kulepheretsa ntchito yoganizira chisamaliro cha chilengedwe.
- Papayo akunenetsa kuti maphunziro okhudza kuwonongeka kwa chilengedwe ndi othandiza kuzindikiritsa anthu za kuipa koononga chilengedwe. Maphunziro amtunduwu akuyenera kuchitika m'malo osiyanasiyana monga m'mabanja, m'sukulu, m'mabungwe ofalitsa mau, m'maphunzitso a katekisirimu, m'mabungwe azandale ndi m'magulu ena monga m'miphakati (213-214).
- Iye akukumbutsa Akhristu kuti Masakramenti ndi masiku Alamulungu ndi ofunikira pofuna kuzindikiritsa anthu za ubale wabwino umene umayenera kukhalapo pakati pa anthu ndi

chilengedwe. (233-237).

- Papayo akusinkhasinkha za ubale umene ulipo pakati pa Utatu Woyera, Maria ndi Yosefe ndi chilengedwe. Akutsiriza maganizo akewa ndi, “pemphero lopempherera dziko lapansi” komanso chilengedwe (238-246).
- Akupempha kuti munthu aliyense atembenuke mtima payekhapayekha komanso ngati gulu lonse la mtundu wa anthu ndi kusiya mtima wodzikonda. Akupemphanso anthu onse kuti akhale ndi makhalidwe oganizira chilengedwe ndi ubwino wa anthu onse. Izi ziyenera kukhudza anthu okhulupirira Mulungu ndi ena onse pa dziko lapansi (202-215).
- Iye akutchulaponso magulu ena a anthu amene ali ndi mtima wongofuna kudziwunjikira zinthu zambiri ndipo amafuna kuwongolera kachitidwe ka malonda osiyanasiyana pofuna kupeza phindu lalikulu ndi kulepheretsa ntchito yoganizira chisamaliro cha chilengedwe.
- Papayo akunenetsa kuti maphunziro okhudza kuwonongeka kwa chilengedwe ndi othandiza kuzindikiritsa anthu za kuipa koononga chilengedwe. Maphunziro amtunduwu akuyenera kuchitika m’ malo osiyanasiyana monga m’ mabanja, m’ sukulu, m’ mabungwe ofalitsa mau, m’ maphunzitso a katekisimu, m’ mabungwe azandale ndi m’ magulu ena monga m’ miphakati (213-214).
- Iye akukumbutsa Akhristu kuti Masakramenti ndi masiku Alamulungu ndi ofunikira pofuna kuzindikiritsa anthu za ubale wabwino umene umayenera kukhalapo pakati pa anthu ndi chilengedwe. (233-237).
- Papayo akusinkhasinkha za ubale umene ulipo pakati pa Utatu Woyera, Maria ndi Yosefe ndi chilengedwe. Akutsiriza maganizo akewa ndi, “pemphero lopempherera dziko lapansi” komanso chilengedwe (238-246).

Momwe Laudato Si' ingagwiritsidwire Ntchito

Nawa maganizo a momwe magulu osiyanasiyana monga maparishi, sukulu, gulu lanu, zipani zamumpingo, ndi magulu ena otero angagwiritsire ntchito kalata ya Papa Francis yotchedwa **Laudato Si'** pofuna kusamalira dziko lathu ndi chilengedwe:

1. Tsatani **Lonjezo la Francis Woyera**

Lonjezani kuti mudzapemphera ndipo mudzachitapo kanthu kothandiza kuthetsa vuto la kusintha kwa nyengo. Kutsata lonjezo la Francis Woyera kudzakuthandizani kuti musamalire bwino dziko lathu ndiponso abale ndi alongo athu amene ali pachiwopsezo.

Kupemphera

- Khazikitsani nthawi **yopempherera** ntchito yothana ndi kusintha kwa nyengo.
- Pempherani ngati banja kapena bungwe la Mpingo (mwachitsanzo: kuchita mapemphero a Akhristu pa mwambo wa Misa)
- Khalani ndi kawundula wa mapemphero anu.
- Sindikizani mapemphero anuwo m'nyuzipepa kapena m'magazini.

Zoyenera kuchita

- Phunzirani momwe kusintha kwa nyengo kumakhudzira anthu **amene ali pachiwopsezo**.
- Onani zomwe **mumachita zodzetsa** mpweya woipa.
- Fufuzani za mphamvu zina zamagetsi monga mphamvu ya dzuwa ndi mphepo.
- Muchitepo **kanthu kothandiza** kuchepetsa mpweya woipa wopangidwa ndi inu.

Kulankhula za vuto la kusintha kwa nyengo

- **Lumikizanani** ndi kulankhula ndi adindo opanga malamulo ndi mfundo zina.

- Lumikizanani ndi kulankhula ndi adindo a ku makhonsolo.
- Fufuzani mfundo zabwino zothandiza kuchepetsa kuwonongeka kapena kusintha kwa nyengo.
- Pemphani wansembe kapena mbusa wanu kuti azilalika za **Laudato Si'** ndi za chisamaliro cha chilengedwe.

2. Kukhazikitsa kapena kulowa m'**bungwe losamalira chilengedwe** Magulu osamalira chilengedwe amathandiza Akatolika kutsogolera pa zochitika zothandiza kuthetsa vuto la kusintha kwa nyengo – limodzi. Gulu losamalira chilengedwe, kaya ndi la ku parishi kaya ndi ku malo ogwirako ntchito kaya kusukulu, likuyenera kugwira ntchito yothandiza kusintha zinthu, kupeza zipangizo ndi kulimbikitsa magulu olankhulapo za mfundo zokhudza kusintha kwa nyengo.

3. Lowetsani nkhani yokhudza kusamalira chilengedwe m'zochitika za parishi, sukulu kapena za m'mudzi mwanu. Mukafuna kudziwa zambiri zokhudza kusamalira chilengedwe m'parishi yanu, mu utumiki wa achinyamata ndipo zokhudza maganizo ena pa nkhanayi, onani pa website ya *Laudato Si'* yomwe ili m'munsiyi:

Vatican.va/content/Francesco/en/encyclicals/documents/papa-francesco_20150524_enciclica-laudato-si.html

Kapena *Laudato Si'*

www.catholicclimatecovenant.org/resources/laudato-si

4. Konzani ndi kuchita **phwando la chaka cha Francis Woyera** Mutu wa Chaka cha Francis Woyera chaka chino ndi ***Dial Down the Heat – Chepetsani Kutentha***: Limbikitsani mfundo yosamalira chilengedwe mokomera anthu onse ndiponso dziko lathu. Zomwe zidachitika m'zaka za 2016 ndi 2017 zikuthandizani kupeza mayankho oyenera okhudza zomwe Papa Francis adapempha kuti pakhale kukambirana za zomwe munthu ayenera kuchita pa nkhani yosamalira chilengedwe cha Mulungu ndi momwe nyengo imakhudzira anthu makamaka osauka.



The Catholic Secretariat
Episcopal Conference of Malawi
P.O. Box 30384
Lilongwe 3

+265 1 721 066
+265 1 772 019
ecm@ecmmw.org